



NTCHISI DISTRICT EXAMINATIONS BOARD

2026 PSCLE DISTRICT MOCK EXAMINATION CHICHEWA (100 MALIKI)

GAWO A (MALIKISI 30)

Langizo:

- Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali mmusiwa. Sakhani chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere 100 komanso asabzole 150.

1. Lembani chimangirizo pa mutu “**PHWANDO LOSAYIWALIKA**”

Mwa zina tsatani izi polemba chimangirizo chanu:

Ndime yoyamba

- Tsiku ndi nthawi yomwe phwando lidachiikira
- Kumalo komwe kudachitikira phwando
- Kuchuluka kwa anthu omwe adabwera ku phwando

Ndime yachiwiri

- Chifukwa chomwe adakonzera phwandoro
- Zinthu zitatu zomwe zidachitika kuphwandoko
- Chomwe chidachititsa kuti phwandolo likhale losaiwalika

Ndime yachitatu

- Perekani malangizo awiri omwe ayenera kutsatidwa pa malo achisangalalo

KAPENA

2. Lembani kalata kwa makolo anu kuwadziwitsa za matenda omwe afala pa sukulu yanu yogonera komweko. Mwazina tsatani izi polemba :

Ndime yoyamba:

- Cholinga cha kalatayo
- Dzina la matendawo
- Tsiku lomwe matendawo adayambira
- Chomwe chidayambitsa matendawo

Ndime yachiwiri

- Chiwerengero cha ophunzira omwe akudwala matendawo
- Chithandizo chomwe odwalawo akulandira

Ndime yachitatu

- Zizindikiro ziwiri za matendawo
- Zinthu ziwiri zomwe mukuchita kuti matendawo asapitilire kufala

DZINA LANU:.....



3. Werengani akhuni yotsatirayi mosamala kwambiri kenako yankhani mafunso otsatirawo:

Panali mudzi wina wotchena Nsisimala womwe mudali banja lina lalitsiro. Banja limeneli lidali la bambo ndi Sauzika ndi mayi Namoyo. M'banjamu mudali ana atatu' amuna awiri ndi wankazi mmodzi. Mwana wachisamaba anatchedwa misolo, chitsitsansepe adali Zilipo ndipo mzime amatchedwa Nasimbenji.

A Sauzika ndi a namoyo adali aulesi ndipo sandathe kuphunzitsa ana awo aja ntchito zosiyansiyana. Anawo sadakule ndi machalidwe abwino. Kawirikawiri amagona ndi njala, moti Misolo, Zilipo ndi Nasimbenji amargokhalira kudya m'makomo mwa anthu ena mpaka adafika poti anthu am'mudzimo adatopa nawo ana aja. Anthu amati akawaona amawapitikitsa ana aja ngati agalu.

Mnyumba mwawo mudali mosasamala ndipo ndipo adalibe chimbudzi. Zinyalalal zidapeza nkuti pakhomo paja ndipo ntchentche zimangoti ng'wang'wang'wa. Chifukwa chosamala pakhomo pawo pamapezeka kuti nthawi ya mvula matenda samachoka. A Namoyo nthawi zambiri ndiye adali bwenzi la mphasa. Ana aja adalibe nthawi yosamba ndipo zovala zawo zidali zaumve.

Tsiku lina kudabwera wa zaumoyo a mangamudzi, Mayi namoyo adawadandaulira kuti ana awo amangodwaladwala ndipo amaonda. A mangamudzi adauza kuti "panyumba pafunika kusesa, kukhala ndi chimbudzi ndi dzenje lotayamo zinyalala. A Namoyo adamva za malangizo koma sadathe kuphunzitsa anawo chifukwa adawalekelera kale.

A sauzika chifukwa cha ulesi adalephera kuchita zomwe a Mangamudzi adawauza.

Tsopano yankhani mafunso

- a. Kodi banja la a Sauzika limakhala mudzi uti? _____ (1mrk)
- b. Kodi ndi mwana uti adali:
 - i. Wotsiriza kubadwa: _____ (1mrk)
 - ii. Woyamba kubadwa: _____ (1mrk)
- c. Tchurani zinthu ziwiri zomwe zikusonyeza kuti banja la Sauzika lidali la umve.
 - i. _____ (1mrk)
 - ii. _____ (1mrk)
- d. N'chifukwa chiyani a Sauzande ndi a Namoyo sanaphunzitse ana awo ntchito? _____ (1mrk)
- e. Perekani matanthauzo amawu awa:
 - i. Nkhuti: _____ (2mrks)
 - ii. Chitsitsansepe : _____ (2mrks)
- f. Lembani mavuto awiri omwe banjali limakumananawo
 - i. _____ (1mrk)
 - ii. _____ (1mrk)
- g. N'chifukwa chiyani a Namoyo adali bwenzi la mphasa? _____ (2mrks)
- h. Kodi a mangamudzi adali ndani? _____ (2mrks)
- i. Kodi ndi malangizo awiri oti omwe a Namoyo adauzidwa ndi a zaumoyo?
 - i. _____ (1mrk)
 - ii. _____ (1mrk)
- j. Kodi dzira loti Sauzika likugwirizana bwanji ndi zochitika m'nkhanayi? _____ 2mrks

GAWO C (MALIKISI 10)

Yankhani mafunso onse awiri m'gawoli

4. Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.

Pakampani panopachuluka akamatule. Ambiri simubwelera ntchito koma kugwetsa kampaniyi ndikuchenjezani kuti yemwe agwire chikho mkati aona chomwe chidameta nkhangampara.

MAFUNSO

a. i. Ndimalonje anji amenewa? _____ (1mrk)

ii. Kodi akuyankhula mnhaniyi ndani?

_____ (1 mrk)

iii. Mawu oti “agwire chikho mkati” akutanthauzani?

_____ (1mrk)

b. Tchurani njira imodzi ingagwiritsidwe ntchito pofuna kusunga chikhalidwe chamakolo

_____ (1mrk)

c. Perekani mwambo umodzi wa makolo omwe ungalimbikitse kufala kwa matenda a EDZI

_____ (1mrk)

5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

a. bwatika

_____ (1mrk)

b. ulalo

_____ (1mrk)

c. mu

_____ (1mrk)

d. mpaka

_____ (1mrk)

e. shomola

_____ (1mrk)

GAWO D (MALIKISI 40)

Zungulizani lembo lokhoza (A,B,C kapena D) mmafunso otsatirwa:

Mafunso 6 mpaka 10. Sankhani mitundu ya maina omwe atsekedwa mzere kungsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi

6. Hi! Buku langa lasowa

A. Mvekero C. Mfuwu

B. Muonjezi D. Mneni

7. Pepala loyera limawala bwino ukalembapo

A. Mfotokczi C. Muonjezi

B. Mneni D. dzina

8. Oterewa ndimakondwera nawo

A. Dzina C. Mfotokozi

B. Mowammalo D. Muonjezi

9. Wakhoza poti umalimbikira

A. Mvekero C. Mneni

B. Mlowammalo D. Mlumikizi

DZINA LANU:

10. Ndatopa chifukwa ndathamanga kwambiri

- A. Mperekezi C. Muonjezi
B. Mneni D. Mfotokozi

Mafunso 11 mpaka 15. Sankhani mitundu ya afotokozi omwe atsekedwa mzere kungsi mziganizo zotsatirazi:

11. Mnyamata wanyonga uja akukankha ngolo

- A. Wamaonekedwe C. Wamwini
B. Wamakhalidwe D. Wamgwirizano

12. Nkhoku zingapo zafa

- A. Wopaula C. Woerenga
B. Wogawa D. Wamgwirizano

13. Vumbwe yeriwe anagwira nkhuu wagwidwa

- A. Waumwini C. wamgwirizano
B. Wowerer ga D. Wogawa

14. Mwana wathawitsa nkhuu zathu

- A. Wogona C. Wauwini
B. Wopatula D. Wamgwirizano

15. Chala ichi chaupa

- A. Wamaonekedwe C. Waumwini
B. Woloza D. Wakuchuluka

Mafunso 16 mpaka 20. Sankhani mawu oyenera kutsiriza ntchedzero zomwe zili m'musizi:

16. Khosi kutalika ngati _____

- A. Kalulu C. Dokowe
B. Galu D. Chilembwe

17. Kusatha kusumbira ngati _____

- A. Mbiya C. Kapu
B. Mwana D. Mkazi

18. Nkhuli ngati _____

- A. Galu C. Mkango
B. Chona D. Fisi

19. Kusakhuta ngati _____

- A. Fulu C. Kumunda
B. Kumanda D. Njoka

20. Kuipa mtima ngati mfiti _____

- A. Yaying'ono C. Yayikazi
B. Yokalan'ba D. Yayimuna

Mafunso 21 mpaka 25. Sankhani mawu omwe akufanana ndi omwe atsekedwa mzere kungsi kwawo.

21. M'munda mwa agogo muli chiwindo

- A. Mtsiriko C. Kholowa
B. Mbewu D. Njoka

22. Balaula akuseera pa mtengo

- A. Galu C. Kalikongwe
B. Chule D. gulugufe

23. Tsomba ndi mbwayokongola

- A. Kwabwanda C. Chitute
B. Mende D. Thondwe

24. Atsikana akunkhumuza chimanga

- A. Peta C. Bzala
B. Tonola D. Konola

25. Agogo ali ndi zifuyo zambiri

- A. Ziweta C. Zingwe
B. Zaka D. Zakudya

Mafunso 26 mpaka 30. Sankhani mtundu wa nthambi yomwe ili ndi mzere kungsi kwake m'ziganizo zotsatirazi:

26. Sindidafunse chomwe iye amafuna

- A. Yadzina C. Yoima payokha
B. Yamuonjezi D. Yamfotokozi

27. Ife tidalira pamene amatulutsa mtembo

- A. Yadzina C. Yamuonjezi
B. Yamfotokozi D. Yoyima payokha

28. Ndipsi yomwe idathyola nyumba ija ayigwira

- A. Yadzina C. Yamuonjezi
B. Yoyima payokha D. Yamfotokozi

29. Mwanayo adakhoza mayeso chifukwa amalimbikira kuwerenga.

- A. Yoyima payokha C. Ya dzina
B. Yamuonjezi D. Yamfotokozi

30. Kuti adalephera mayeso ndi zoon

- A. Yoyima payokha C. Yamuonjezi
B. Ya dzina D. Ya mfotokozi

Mafunso 31 mpaka 35. Sankhani matanthauzo oyenera azining'a zomwe zili ndi mzere kungsi kwake mziganizo zotsatirazi:

31. Bamboo dalireni ndi a Kambona mmudzi mwathu

- A. Kapolo C. Wolimba mtima
B. Wosauka D. Wolemera

32. Popita kwa agogo ndidzagwira tambala pakhozi

- A. Kutenga nkhuu C. Kuyenda wapasi
B. Kulawilira D. Kuyenda pagalimoto

33. Mariya adakwantiwa pantchafu pa mudzi uwo.

- A. Adakwatira ndi mbava
B. Adakwatiwa ndi wolemera

DZINA LANU:

- C. Adakwatiwa ndi mfumu
D. Adakwatiwa ndi wosauka
34. Mnyumba ya a Nambewe mulibe nsalu
yalekaleka
A. Mwamuna C. Mwana
B. Bambo D. Mayi
35. Nabanda ndi Kamchacha . lero ali ku Malawi
A. Oyendayenda C. Hule
B. Wokongola D. Wodanitsa
- Mafunso 36 mpaka 40. Sankhani magulu amayina omwe atsekedwa mzere kungsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**
36. Ndege yafika chakummawaku
A. U – MA C. Chi – ZI
B. I – ZI D. Mu – A
37. Tisabwe tavuta zedi mnyumba mwanga.
A. Chi – ZI C. LI- MA
B. U – MA D. Chi – ZI
38. Mbewa yalo wa ku una
A. U – MA C. LI _ MA
B. KA – TI D. CHI – ZI
39. Kusewera mkopindulitsa pa moyo wa munthu
A. MU – M
B. Ku + tsinde la mneni
C. Ku – Pa – Mu
D. I – ZI

40. Atsikana akucheza m'nyumba mwawo
A. MU – MI C. Li – MA
B. MU – A D. KU – PA - MA

Mafunso 41 mpaka 45. Sankhani mayina omwe akusonyeza kuchuluka kwa mayina omwe ali ndi mzere kungsi kwawo.

41. Mbuzi zodya chimanga chonse
A. Dzimanga C. Vimanga
B. Chimanga D. Pamanga
42. Tsaya langa latupa
A. Masaya C. Dzimasaya
B. Matsaya D. Vimasaya
43. Ana akusewra pa chulu
A. Chulu C. Machulu
B. Zulu D. Vichulu
44. Mwana wagula ndazi
A. Mandazi C. dzindazi
B. Zindazi D. Mandasi
45. Bongololo wafa
A. Mabongololo C. Vibongololo
B. Bongololo D. Abongololo

MAFUNSO ATHERA PANO

